# ULOSI NDI MBIRI YA DZIKO LAPANSI




**LERO LINO** zizindikiro za nthawi zikutsimikizira kuti tafika pamapeto a chisomo cha Mulungu ndi zochitika zonse zotsutsana ndi choonadi. Zikuoneka kuti dziko lonse liri m'chisokonekero. Tikuuona ulauli wa Yesu wonena za zochitika za nthawi ya pafupi penipeni pa Kubwera kwake Kwachiwiri zikukwaniritsidwa: "Koma inu mudzayamba kumva za nkhondo, ndi mbiri za nkhondo ….. Pakuti mtundu umodzi wa anthu udzaukirana ndi mtundu wina … Ndipo kudzakhala njala ndi zibvomezi m'malo akuti akuti. Koma ndizo zonsezi zowawa zoyamba." (Mateyu 24:6-8). Zochitika panopa komanso za mtsogolomu zikuchititsa chidwi mtundu wonse wa anthu. Ambiri ayamba kuzindikira tsopano kuti chinthu china chachikuru ndi choopsya chatsala pang'ono kwambiri kuchitika; ndi kuti dziko lapansi layandikitsitsa kuchionongeko chachikuru. Nkhani za tsiku ndi tsiku ndi za ngozi za dzidzidzi ndiponso makangano a mitundu mitundu. Yesu analosera izi kuti mu nthawi ya kumapeto kudzakhala "… chisauko cha mitundu ya anthu, alikuthedwa nzeru…" ndi "anthu akukomoka ndi mantha, ndi kuyembekezera zinthu zirinkudza ku dziko lapansi. .." (Luka 21:25-26).

## *ULOSI WODABWITSA WA MAUFUMU AKULUAKULU A DZIKO LAPANSI*

M'Bukhu Lopatulika, makamaka m'mabukhu a Danieli (Dan.)ndi Chibvumbulutso (Chibv.) zochitika zokhuza mbiri ya dziko ndi momwe zinthu ziriri pakali pano zinalaulidwa momveka bwino. Kuwerenga ndi kuwamvetsetsa bwino mabukhu amenewa kukutithandiza ife kuona cholinga cha Mulungu mu mbiri ya anthu a mitundu yonse. Zikutithandiza kumvetsetsa za tanthauzo lenileni ndi cholinga cha moyo ndi nthano ya maomboledwe a mtundu wonse wa anthu kudzera mwa Mwana wake Yesu Khristu. Zaka 2600 zapitazo, mneneri Danieli analosera za maufumu akuluakulu a dziko lapansi, omwe ndi a Babulo, Amedi ndi Aperezi, Ahelene (Greece), Aroma, komanso za dziko lomwe likudziwika kuti Ulaya (Europe). M'maloto Danieli anaona fano lalikuru lomwe zigawo za thupi lake zikuimira ndondomeko ya maufumu'wa motere: "Fano ili tsono, mutu wake unali wagolidi wabwino, chifuwa chake ndi manja ake za siliva, mimba yake ndi chiuno chake zamkuwa, miyendo yake yachitsulo, mapazi ake mwina chitsulo mwina dongo." (Dan. 2:32-33). Maufumu akuruakuru a dziko lapansi'wa ndi makhalidwe ao anaonetsedwanso kwa mneneriyu akuimiridwa ndi zirombo motere: "Zirombo zazikuru izi zinai ndizo mafumu anai amene adzauka ….." (Dan. 7:17). Awa anaonetsedwanso ngati "….mphepo zinai za mumlengalenga zinabuka pa nyanja yaikuru." (Dan. 7:2). Pa Chibv. 17:15 akufotokoza kuti "madzi" akuimira anthu, makamu, mitundu ndi manenedwe," pamene "mphepo" zimaimira "nkhondo" (Yeremiya 4:11-16). Mphepo zinai za mumlengalenga, zomwe zinabuka pa nyanja yaikuru zikuimira kulimbana komwe kunakhala kukuchitika kuti uli wonse wa maufumuwo ulamulire.



### BABULO

Mutu wa golidi ndi mkango (chizindikilo chodziwika bwino cha Babulo) kuimira Ufumu wa dziko lonse lapansi wa Babulo (608-538 BC). Mapiko a chiombankhanga kuimira liwiro ndi mphamvu zakugonjetsa za Nebukadenezara.

Dan. 7:4 Chirombo choyamba chinali ngati Mkango nichikhala ndi mapiko achiombankhanga.

### AMEDI NDI APEREZI

M'chaka cha 538 BC Ufumu wa anthu a mitundu iwiri, Amedi ndi Aperezi unakhazikitsidwa. Mbambo zitatu mkamwa mwa chimbalangondo zikuimira kugonjetsa kumene ufumu wa Amedi ndi Aperezi unakuchita pa maiko atatu: Ludia, Babulo ndi Aigupto. (Kutundumuka mbali imodzi kukuimira Aperezi omwe anali mtundu wa mphamvu ndi kulamulira kwa nthawi yaitali).

Dan. 7:5 Chirombo chachiwiri chinali ngati Chimbalangondo. Chinatundumuka mbali imodzi chinali ndi nthiti zitatu mkamwa mwake.

### AHELENE (GREECE)

Chipambano chamsangamsanga pa nkhondo (mapiko anai) pansi pa Mfumu yaikuru Alexander chinalipanga dziko la Ahelene kukhala ulamuliro wa mphamvu pa dziko lapansi (331 BC). Pambuyo pa imfa ya Alexander ufumuwo unagawika panai pansi pa anai a atsogoleri a za nkhondo ake motere: Thrace, Syria, Macedonia, ndi Egypt (choncho mitu inai).

Dan. 7:6 Chirombo chachitatu chinali ngati Nyalu gwe, yemwe anali ndi mapiko anai ngati a mbalame pa msana pake.

### UFUMU WA AROMA

M'chaka cha 168 BC, Aroma anakhazikitsa ufumu wachinai wa dziko lonse lapansi. Chifukwa chakuchita mwa nkhanza ndi mwa mphamvu pogonjetsa maufumu a mafuko ena, ufumu uwu unadziwika ndi dzina lakuti "Ufumu wa Chitsulo." (Kumbukirani za miyendo ndi mano za chitsulo za chirombochi).

Dan 7:7 Chirombo cha chinai chinali choopsa ndi chochititsa mantha ndi cha mphamvu kwambiri. Chidali ndi mano aakuru a chitsulo; chinalusa ndi kuphwanya ndi kupondereza… Chinali ndi nyanga khumi.

### MAIKO A KU ULAYA (EUROPE)

Chifukwa cha misamuko (351-476 AD), Ufumu wa Aroma unagawika m'maufumu khumi a ku Ulaya. (Kumbukirani nyanga Khumi ndi zala khumi). Kugawanika kwa nyanga khumi ndi kusaphatikizana pamodzi kwa zala khumi kukuimira kusatheka kwa mgwirizano wokhalitsa wa maulamuliro a ku Ulaya.

Dan 7:24 Nyanga khumi ndizo mafumu khumi amene Adzauka kuchokera mu ufumu uwu.

## UFUMU WA DZIKO LAPANSI WOSIYANA NDI OYAMBA'WO

NDIPO MNENERI anaona ufumu wina ukuphuka m'Ulaya: "Ndinali kulingirira za nyangazi, taonani, pakati pa izo inaphuka nyanga yina." (Dan. 7:8). Ulamuliro uwu unali ndi zizindikiro izi:

1. IKUPHUKA PAKATI PA NYANGA KHUMI (Dan. 7:8).

Ulamuliro wa Upapa (508 AD) ndiwo unali "nyanga yaing'ono, " unauka pakati pa mafuko khumi a mtundu wa chi-German.

2. IZULA NYANGA ZITATU (Dan. 7:8).



A Heruli, ma Vandal ndi a Ostrogoth analimbana ndi ulamuliro wa "nyanga ya ying'onowu ndipo "anazulidwa ndi mizu yomwe" – m'mau ena anthu ao anaphedwa onse osasiya ndi wa mbeu yemwe.

3. ISIYANA NDI NYANGA ZOYAMBA (Dan. 7:24).

Ulamuliro wa Papa unali wosiyana kotheratu ndi oyamba aja. Unali wophatikiza pamodzi za Chipembedzo ndi za ndale; chipembedzo chinayendetsa ndale.

4 . NDI YA MPHAMVU KUPOSA NYANGA ZOYAMBA (Dan. 7:20).

Ulamuliro wa Papawu unakula mofulumira m'kanthawi kochepa nukhala wa dziko lonse lapansi. M' nthawi ya "Zaka za Mdima," anthu analandira chikhulupiriro cha chipembedzo cha chi-Katolika m'machitidwe okakamiza (moumirizidwa).

5. IDZIKUZA NDI KULANKHULA ZOCHITIRA MWANO MULUNGU (Dan. 7:25).

"Adzaukiranso kalonga wa akalonga" (Dan. 8:25). Iye ali "mwana wa chionongeko, amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zotchedwa Mulungu, kapena zopembezeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku Kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu." (2 Atesalonika 2:3-4) Malemba atatu onsewa akunena za ulamuliro umene umadzionetsera kuti ndi wa Chikhristu, chikhalirecho uli wotsutsana ndi chikhristucho m'malingaliro ake. Zolembera izi zikuonetsera poyera choonadi cha mwano umene ulamulirowu wakhala ukuchitira Mulungu: "Pa dziko lapansi pano tiri m'malo mwa Mulungu Wam'mwambamwamba." (Encyc. Pope Leo XIII, 6-20-1894.) Kumutcha Papa ndi mau akuti "Atate Woyera" ndi mwano waukuru kwa Mulungu. Yesu anachenjeza za ichi pa Mateyu 23:9 "Ndipo inu musatchule wina atate wanu pansi pano, pakuti alipo mmodzi ndiye Atate wanu wa Kumwamba." Mosafuna kumvera malangizo a m'Bukhu Lopatulikawa, apapa ambiri m'zaka zonse zapita m'mbuyomu akhala akudzinena kuti ndi osachimwa, sanachimwepo ndipo sadzachimwa, khalidwe lomwe ndi la Mulungu yekha osati munthu ai (Chibv. 15:4), ndipo kuonjezera apo adzitengera mphamvu ingakhale yokhululukira machimo yomwe ndi ya Mulungu yekha (Luka 5:21).



6. IZUNZA OYERA MTIMA A WAM'MWAMBAMWAMBA (Dan. 7:25).

Kukhazikitsa ankhondo olimbana ndi otsutsana nao, kutengera otsutsana nao ku mabwalo milandu, kuwazunza mu nyumba za ndende, ndi kuwaponya ali moyo mung'anjo kapena mafuta a moto ndi mchitidwe woipitsitsa umene ndi wosaiwalika tikamanena za ulamuliro wa Papa. Wolemba Mbiri yakale W.H. Lecky akuti, "Kuti Mpingo wa Romu unakhetsa mwazi wochuruka wa anthu osalakwa kuposa bungwe lina liri lonse lomwe linakhalapo chilengedwere cha dziko lapansi, si chinthu chimene chingatsutsidwe ndi munthu ali yense amene ali ndi chidziwitso chokwanira za mbiri yakale … Chiwerengero chenicheni cha anthu amene anazunzidwa sichikudziwika (chingathe kukhala pafupifupi

miyanda makumi asanu [50, 000,000]), ndipo palibe ali yense angathe kumvetsetsa za mazunzo omwe anthuwo anadutsamo.” Rationalism in Europe, Vol. 2, page 32).

7. IYESA KUSINTHA NTHAWI NDI CHILAMULOCHO (Dan. 7:25).

Ulamuliro wa Papa unayesetsa kusintha lamulo la Mulungu. Unachotsa lamulo lachiwiri la malamulo khumi mu Katekesimo wa Chikatolika. Lamulo lachiwiri likuletsa kupembedza mafano. Unasintha lamulo lachinai la Mulungu, lonena za kusunga Sabata loyera la m’Bukhu Lopatulika (Saturday), kukhala Sunday, lomwe magwero ake ndi a chipembedzo cha chikunja cha Dzuwa. M’malo mwa Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mulungu molingana ndi lamulo lachinai la Mulungu (Eksodo 20:8-11; Yesaya 56:2-7), Sunday linakhazikitsidwa, motsutsana ndi Bukhu Lopatulika kukhala lopumula. Mulungu sanalamulire pena pali ponse kuti tsiku loyamba la pa mulungu lidzikhala lopembedza ndipo Yesu ndi ophunzira ake sanasungepo Sunday (Luka 4:16; Mat. 24:20; Machitidwe 13:42-44).

8. ILAMULIRA NTHAWI IMODZI, NDI NTHAWI ZINA NDI NTHAWI YA NUSU (Dan 7:25).

Mu kawerengedwe ka ulosi, liu “nthawi” limaimira chaka chimodzi chokhala ndi masiku 360. Choncho nthawi 31/2 = zaka 31/2 = masiku 1,260. Mu ulosi tsiku limaimira chaka chimodzi (Ezekieli 4:6; Numeri 14:34).


Choncho “nyanga yaing’ono” idzalamulira kwa zaka 1,260. Nthawi’yi inayamba pamene mfumu Justinian (anapereka ulamuliro wa za ndale ku mpingo wa Romu kuonjezera pa utsogoleri wake wa za uzimu) ndiponso kuonongedwa kwa Ufumu wa ku M’mawa wa a Goth m’chaka cha 538 A.D. Inatha m’chaka cha 1798 ndi undende wa Papa Pius VI nthawi yomwe mtundu wa boma wa dziko la Romu unasintha kukhala Republic womwe atsogoleri amachita kusankhidwa ndi anthu womwe unayambitsidwa ndi Napoleon, mkuru wa nkhondo wa chi – French osati maufumu monga zimakhalira pa chiyambi.



# NTHAWI YA CHIWERUZIRO

“KOMA WOWERUZA MLANDU ADZAKHALAKO…” (Dan. 7:26). Danieli anapenyerera “mpaka anaikapo mipando ya chifumu, nikhalapo Nkhalamba ya kale lomwe …. Zikwi zikwi anamtumikira, unyinji wosawerengeka unaima pamaso pake, woweruza mlandu anakhalapo, ndi mabuku anatsegulidwa.” (Dan. 7:9-10). Umu ndimo anaonetsedwera masomphenya za tsiku lalikuru ndi loopsa pomwe makhalidwe ndi moyo wa munthu ali yense ayenera kudzaweruzidwa pamaso pa Woweruza wa dziko lonse lapansi.

Lemba likunena kuti, “mabuku anatsegulidwa.” Mneneri Yohane akufotokoza mopitiriza kuti, “Ndipo bukhu lina linatsegulidwa, ndilo la moyo. Ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m’mabuku, monga mwa ntchito zao” (Chibv. 20:12). Mabukhu a chikumbutso kumwamba, momwe maina (Luka 10:20) ndi ntchito (Mateyu 12:36-37) za anthu zalembedwa ndiwo adzagwiritsidwa ntchito pa chiweruzo. Zinsinsi ndi zolingirira zonse zidzaululidwa mu zolembera zosaphophonyazo, pakuti Mulungu adzaika poyera zinthu zonse zobisika “nasonyeza zitsimikizo za mtima.” (1 Akorinto 4:5). Ndipo Iye “adzanena mlandu wa zoipa zonse, ndi zobisika zonse, ngakhale zabwino ngakhale zoipa.” Mlaliki 12:14.



Pamene mabuku a chikumbutso adzatsegulidwa opembedza Mulungu onse adzafufuzidwa. “Chifukwa yafika nthawi kuti chiweruziro chiyambe pa nyumba ya Mulungu; koma ngati chiyamba ndi ife, chitsiriziro cha iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Mulungu chidzakhala chiyani?” (1 Petro 4:17).

Khristu anayamba chiweruziro cha kufufuza ndi iwo amene anayamba kukhala ndi moyo pa dziko lapansi. Kenaka ndi anthu amibadwo yonse, ndipo akutsirizira ndi chiweruziro cha anthu amoyo. Dzina liri lonse likutchulidwa, ndi mlandu wa munthu ali yense ukufufuzidwa mosamalitsitsa. Maina akubvomerezedwa, ndi ena akukanidwa. Lamulo la Mulungu ndilo muyeso womwe ntchito ndi moyo wa anthu zikuyezedwa nalo mu nthawi ya chiweruziroyi. Bukhu Lopatulika likufotokoza bwino za chiweruziro’chi pakunena, “lankhulanani motero, ndipo chitani motero, monga anthu amene adzaweruzidwa ndi lamulo (Malamulo Khumi) la ufulu.” (Yakobo 2:12).

Ngati pali anthu amene machimo ao sanalapidwe ndi kukhululukidwa, oterowo maina ao adzachotsedwa m’Bukhu la Moyo. Ambuye akutsimikizira ichi ndi mau akuti, “Iye amene wandichimwira, ndifafaniza yemweyo kumchotsa m’bukhu langa.” (Eksodo 32:33) Onse amene moona mtima alapa machimo (Miyambo 28:13) ndipo mwachikhulupiriro alandira mwazi wa Khristu kukhala nsembe yowatetezera (Machitidwe 16:30-31) palembedwa chikhululukiro pa maina ao m’mabuku a kumwamba. Tsono popeza akhala oyera monga Khristu ali woyera (1 Yohane 2:29) ndipo makhalidwe ao ali ogwirizana ndi lamulo la Mulungu, machimo ao adzachotsedwa ndipo iwo adzakhala oyenera moyo wosatha. Ambuye kudzera mwa mneneri Yesaya akuti: “Ine, Inedi, ndine amene ndifafaniza zolakwa zako chifukwa cha Ine mwini; ndipo Ine sindidzakumbukira machimo ako.” (Yesaya 43:25). Umu ndimo zinthu zidzakhalire pa kuuka kwa olungama monga kwalembedwa m’ Mau a Mulungu kuti, “Nadzaturukira, amene adachita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adachita zoipa kukuuka kwa kuweruza.” (Yohane 5:29; 1 Atesalonika 4:14-16). Kudzera mwa mneneri Yohane Yesu anati, “Iye amene alakika adzambveka motero zobvala zoyera; ndipo sindidzafafaniza ndithu dzina lake m’bukhu la moyo, ndipo ndidzabvomereza dzina lake pamaso pa Atate wanga, ndi pamaso pa angelo ake.” (Chibv. 3:5). Kupembedzera munthu kwa Khristu pampando wachifumu wa Atate wake kumwamba (Ahebri 8:1) ndi kofunikira kwambiri pa ndondomeko ya chipulumutso monganso idali imfa yake ya pa mtanda (Ahebri 9:24). Yesu anatsegula njira yaku mpando wachifumu wa Atate wake, ndipo kudzera mu ntchito yake ya Umkhalapakati, zolingirira zolungama za onse akudza kwa Iye mwa chikhulupiriro zimafika pamaso pa Mulungu. “Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa.” (Ahebri 4:16). Yesu akutitetezera ife chifukwa cha manja ake olasidwa ndi thupi lake lotundudzidwa, ndipo akuuza ali yense wofuna kumtsatira Iye: “Chisomo changa chikukwanira” (2 Akorinto 12:9). “Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; chifukwa ndiri wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wopepuka.” (Mateyu 11:29-30).

Pa nthawi yomwe chikumbu mtima chathu chimadzudzulidwa ndi Mzimu Woyera, timazindikira mphamvu, kuipa, ndi chisoni zakudza chifukwa cha uchimo ndipo timadza komwe tingathe kulapa. Zimatheka kuoneka kwa ife ngati kuti uchimo watilekanitsa ndi Mulungu, ndi kuti tiri pansi pa ukapolo wa woipayo. Pamene tiyesetsa mwa umunthu kudzipulumutsa mu uchimo ndi pomwe timaipiraipira.Kenaka tikalingirira mwakuya timapeza kuti moyo wathu wadzala ndi kudzikonda ndiponso uchimo; ndipo timayamba kumva kufunikira kwa kukhululukidwa, kuyera mtima ndiponso ufulu. Timayamba kudzifunsa, Ndingachite chiyani kuti ndiyanjanenso ndi Mulungu? Timapeza kuti timasowa chilimbikitso, chikhululukiro cha machimo chochokera kumwamba, mtendere ndiponso chikondi mu mtima mwathu. Zonsezi’tu sizingagudwe ndi ndalama, mphamvu kapena nzeru, koma, Mulungu amapatsa izi kudzera mu mphatso ya ulere ya chisomo: “…inde, idzani, mugule vinyo ndi mkaka opanda ndalama ndi opanda mtengo wake” (Yesaya 55:1). Zanenedwazi zingatheke pa ife ngati ife titatsegula mitima yathu ndi kuzilandira. Mulungu akutsimikizira: “…ngakhale zoipa zanu ziri zofiira, zidzayera ngai matalala” (Yesaya 1:18). “Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga mkati mwanu mzimu watsopano” (Ezekieli 36:26). Titatha ife kuzindikila ndi kubvomereza zochimwa zathu, timalimbikitsidwa kuyamba moyo watsopano mwa Mulungu. Pamenepo timadza ndi kumpempha Iye kuti atitsuke machimo athu ndi kutipatsa mtima watsopano. “Ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse.” (1 Yohane 1:9; Miyambo 28:13). Tikhale ndi chikhulupiriro chakuti Mulungu angathe kutichitira izi zonse chifukwa Iye analonjeza. Ichi ndicho Khristu anachiphunzitsa pamene anali pa dziko lapansi pano, kuti mphatso yolonjezedwa kwa ife ndi Mulungu ndi yathu ngati titailandira mwachikhulupiriro. Ife sitingathe kudziyeretsa tokha ku machimo athu, sitingaisinthe mitima yathu komanso kulandira chipulumutso mwa ntchito za ife eni (Yeremiya 13:23; Aefeso 2:8). Koma Mulungu analonjeza kuti adzatichitira ichi kudzera mwa Khristu. Ife tikhulupirire lonjezano’lo; tibvomereze machimo athu, tidzikhuthule kwa Iye ndi kumtumikira. Tikangochita ichi, Iye adzakwaniritsa lonjezano lake kwa ife. Yesu adzapitiriza kukhala Nkhoswe ndi Mtetezi wathu: “Akachimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Yesu Khristu wolungama; ndipo Iye ndiye chiombolo cha machimo athu; koma osati athu okha, kamanso a dziko lonse lapansi.” (1 Yohane 2:1-2).

# UTHENGA WOTSIRIZA WA CHIFUNDO



Dan. 2:34 . . . kufikira mwala . . . unagunda fanoli pa mapazi ake . . . nuwaphwanya.

**Mneneri** Danieli anaonetsedwa kuti pa nthawi imene anthu a ku Ulaya adzidzayesera kupanga mgwirizano, dziko lapansi lidzakhala liri m’zisautso ndi nkhondo, ndipo mwala waukuru udzamenya ndi kuphwanya mapazi a fano ndi kulionongeratu. Mwala’wo ukuimira Kubwera kwa Yesu Khristu (Dan. 2:34-35, 44; Masalmo 18:32). Khristu akubweranso posachedwa m’mitambo ya kumwamba ndi angelo ake, moonekera kwa anthu onse (Chibv. 1:7). Choncho pofuna kuwakonzetsera anthu za kubwera kwakeko ndi kuwathandiza kuti adzathe kuima pa chiweruziro, Mulungu, mwa chikondi chake, akuchenjeza anthu onse ndi uthenga wotsiriza wachifundo chake wopezeka pa Chibvumbulutso 14:6-12.



## UTHENGA WA MNGELO WOYAMBA

***WOYAMBA*** — "Opani Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake; ndipo mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe a madzi" (Chibv. 14:6-7).

Uthenga wa mngelo woyamba ukutiuza ife kuti timvetsetse kuti chiweruziro chikuchitika mu nthawi ino kumwamba, chifukwa kuchokera chaka cha 1798 mpaka nthawi yapafupi penipeni pakubweranso kwa Khristu, ndi nthawi yomweyomweyo chiweruziro chikuchitika. Ndi mu nthawi yomweyomweyo mtundu wa anthu ukuuzidwa kulambira Mulungu, Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi. Koma ingakhale zinthu ziri choncho, anthu ochuruka akukhulupirirabe zikhulupiriro za bodza zakuti si Mulungu amene



analenga zinthu zonse. Koma Mulungu mwa chifundo chake akufunitsitsabe kuti munthu adziwe za ubwino ndiponso zodabwitsa za ndondomeko ndi malamulo ake a chilengedwe kuti zinapangidwa ndi Iye osati kuti "zinangokhala" mwa ngozi (Werengani Aroma 1:20-21). Iye akumkumbutsa munthu kuti ndi iye amene amagawa mphatso zonse ndipo nkoyenera kuti tidzimkonda ndi kumpatsa ulemu. Chikondi chenicheni pa Mulungu ndicho kupembedza koona komwe ndiko kusunga malamulo ake [Malamulo Khumi monga alembedwera pa Eksodo 20:1-17] "Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake" ndi "Wopewetsa khutu lake kuti asamve chilamulo, ngakhale pemphero lake linyansa" (1 Yohane 5:3; Miyambo 28:9). Kumpatsa Mulungu ulemu kutanthauza kulionetsera khalidwe lake m'makhalidwe athu. Khalidwe la Mulungu limaonetsedwa mwa munthu kudzera m'Malamulo a Mulunguyo.

### CHIZINDIKILO CHA MULUNGU

Lamulo la chinai la Malamulo Khumi limamuonetsera Mulungu mwachindunji kuti ali Mlengi: "Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale lopatulika… Chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamaliza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika" (Eksodo 20:8-11). Lamulo ili ndi lokhalo m'malamulo khumi lomwe likunena za dzina, udindo ndiponso malo amene ulamuliro wa Mulungu ukuchitikira. Izi ndizo zikulipanga lamulo'li kukhala "Chizindikilo cha Mulungu."

Sabata linapangidwira mtundu wonse wa anthu ku nthawi ndi mibadwo yonse n'chifukwa chake linaperekedwa pa Chilengedwe (Genesis 2:1-3). Tsiku ili linaperekedwa kukhala chotikumbutsa pafupipafupi kuti tisaiwale Mlengi




wathu kumtumikira ndi kumlemekeza Iye m'zothokoza. "Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale lopatulika." Kusunga tsiku la Sabata ndi chizindikilo chakukhala omvera pamaso pa Mulungu woona: "Ndipo ndinawapatsanso masabata anga akhale chizindikilo pakati pa Ine ndi iwo, kuti adziwe kuti Ine Yehova wakuwapatula" (Ezekieli 20:12; Yesaya 56:2 Eksodo 31: 13-17).

Kuyambira pa chiyambi pa chilengedwe Sabata la pa tsiku la chisanu ndi chiwiri la pa mlungu lakhala likusungidwa pa Saturday. Yesu mwini wake akufotokoza za umuyaya wa Malamulo Khumi: "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri; sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo kufikira zitachitidwa zonse." (Mateyu 5:17-18).

## UTHENGA WA MNGELO WACHIWIRI

***WACHIWIRI*** — "Wagwa, wagwa, Babulo waukuru umene unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake" (Chibv. 14:8).

Liu "Babulo" likuchokera ku liu "Babele" ndipo likutanthauza "chisokonekero." M'Bukhu Lopatulika liu'li likuimira zipembedzo zosiyanasiyana zonama ndiponso zopandukira Mulungu.

M'Chibvumbulutso 17:4-6 Babulo akufotokozedwa kuti ndi mkazi wachigololo. M'Bukhu Lopatulika, mkazi wachigololo amaimira mpingo (chipembedzo) wopandukira Mulungu (Yeremiya 3:20; Ezekieli 16:35). Mkazi uyu wa chigololo wa pa Chibvumbulutso 17:4-6 "anabvala chibakuwa, ndi mlangali, nakometsedwa ndi golidi, ndi miyala ya mtengo wake, ndi ngale, nakhala nacho m'dzanja lake chikho cha golidi chodzala ndi zonyansitsa ndi zodetsa za chigololo chake….Ndipo pamphumi pake padalembedwa dzina, CHINSINSI, BABULO WAUKURU, AMAI WA ACHIGOLOLO." Mneneri akupitiriza kunena, "Ndipo ndinaona mkazi woledzera ndi mwazi wa oyera mtima, ndi wa mboni za Yesu." Babulo akupitirira kufotokozedwa kuti ali "Mudzi waukuru (wokhala pa mapiri asanu ndi awiri, Ndime 9), wakuchita ufumu pa mafumu a dziko." (Chibv. 17:18).



### CHINSINSI BABULO

Ulamuliro ukunenedwa pano si wina koma wa Romu wa chipembedzo, mzinda wa mapiri asanu ndi awiri. Mlangali ndi chibakuwa zikuimira mitundu ya zobvala za ansembe akuru ndi a episkopi. Golidi, miyala ya mtengo wake ndi ngale zikuimira ulemelero ndi chuma zimene ulamuliro wa pansi pa Papa'wu ulimo. Palibenso ulamuliro wina ungafotokozedwe kuti mkazi, "woledzera ndi mwazi wa oyera mtima" kutanthauza mpingo umene unazunza otsatira a Khristu ndi kuwapha ena mwa nkhanza mopanda chisoni kuposa uwu (werengani tsamba 1ndi 2). Tchimo lalikuru lomwe Babulo akukhuzidwa nalo kwambiri ndilo: "unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake." Chikho chokwiyitsa Mulungu



chimene mkaziyu akuchipatsa ku dziko lapansi ndicho ziphunzitso zonama, zomwe ndi ukaristiya, kuti munthu akafa amakwera kumwamba nthawi yomweyo, chilango cha myaya ku gehena wa moto, kupembedza Mariya, ndi kusunga Sunday kukhala lopatulika. Mpingowu wakhala ukuphunzitsa ziphunzitso izi ndi zina zonse zosakhala za m'Bukhu Lopatulika koma za chikoka chake choipa chotsogolera dziko lapansi ndi mipingo ina ku chionongeko.

Chenjezo lomwe likuperekedwa apa lakuti, "Babulo wagwa" likukhuza magulu onse a mipingo ndi dzipembedzo omwe pachiyambi anali angwiro koma tsopano agwa. Chenjezo'li silikuperekedwa ku mpingo wa Romu wokhawo ai, uwu wakhala uli wakugwa ndi kale lonse ndipo ukudziwika ndi mau akuti Babulo "amai wa achigololo."

Ana ake a akazi akuimira mipingo imene yakakamirabe kuziphunzitso za mpingo wa Romu'wu (mwachitsanzo kusunga Sunday kukhala lopatulika) potsatira chitsanzo chake. Choncho, liu Babulo (chisokonekero) likunena za mipingo imeneyo. Koma ingakhale zinthu ziri choncho ndi mipingo yakugwayo, ambiri a ophunzira enieni a Khristu akadali m'menemo." Ana onse a Mulungu amene akadali m'Babulomu posachedwapa adzamva ndi kusinthika mtima ndi uthenga wa mngelo uwu wakuti "Babulo wagwa" ndi wa"Turukani m'menemo anthu anga," ndipo adzachoka m'mipingo yopandukira Mulunguyo.

## UTHENGA WA MNGELO WACHITATU

***WACHITATU*** — "Ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu…" (Chibv. 14:9-10).

Kuti timvetsetse bwinobwino za uthenga uwu tiyambe ndi kumasulira zomwe maina ophiphiritsa'wa akutanthauza.

### CHIROMBO

Chirombo chomwe chatchulidwachi chikufotokozedwanso pa Chibvumbulutso 13:1-10 kuti, "chinafanana ndi nyalugwe." Pochifanizira "chirombo'chi" ndi "nyanga yaing'ono" ya m'Danieli 7 (werenganinso masamba 1-2) zikuoneka kuti chiri ufumu umodzimodzi womwewo, wodziwika ndi mau akuti Ulamuliro wa Papa.



Monga momwe inali "nyanga yaing'ono," "chirombo" ichinso chikuimira ulamuliro umene ukuchitira Mulungu mwano (Chibv. 13:6) womwenso ukuzunza akhristu (Chibv. 13:7) komanso unachokera mu ulamuliro wa Romu wa Chikunja (Chibv. 13:2), nulamuliranso kwa zaka 1,260 (Chibv. 13:5). Pakutha kwa nthawi ya zaka 1,260 ulamuliro wa chirombochi unafika pa mapeto pokhala ndi "bala la ku imfa" (Chibv. 13:3,10); werengani tsamba 2, pa mutu wa 8). Koma popita kwa nthawi bala la ku imfa'li lidzapola (Chibv. 13:3). Kupola kwa bala la kuimfa la ulamuliro wa Papawu kunayamba m'chaka cha 1929 pa kukhazikitsidwa kwa mgwirizano wa ku Lateran. Pa nthawi imeneyo Vatican analandira katundu wake, chithandizo cha ndalama, ndi kukhala ndi ufulu wokhala ndi a kazembe ku maiko ena monga limachitira dziko liri lonse loima palokha. Kudzera mu mgwirizano wake ndi maiko a dziko lapansi ndiponso kulemera pa chuma Vatican wabwereranso kukhala wa mphamvu ndi chikoka. "Bala laku imfa" likunka likupola.



Tisanapitirire kuona za "Fano la chirombo" ndi "chizindikilo" chake, tiyambe taonanso za ulamuliro wa chirombo china womwenso wafotokozedwa pa Chibvumbulutso 13.

### CHIROMBO CHACHIWIRI

Mneneri akuti, "…ndinaona chirombo china chirikuturuka pansi, ndipo chinali nazo nyanga ziwiri ngati za mwana wa nkhosa…" (Chibv. 13:11).

Pamene chirombo choyamba chija chinaturuka "m'nyanja" yomwe ndi "makamu ndi manenedwe" (Chibv. 17:15), chirombo chachiwirichi "chinaturuka pansi." M'malo mogonjetsa maulamuliro ena kuti chikhazikitse ulamuliro wake, ulamuliro womwe ukutchulidwa apawu unangouka ndi kukula pang'onopang'ono, mwa mtendere ndi mosadzikuza kuchokera m'mafuko olimbanalimbana a ku Ulaya. Unauka ku dziko la kumadzulo. Ndi ulamuliro umodzi wokha womwe ulosi ukuufotokoza mwa chindunji ndipo ukukwaniritsa madzedwe a Ufumu wa dziko la Mgwirizano wa Maiko a ku America (USA) umene unakhala kumapeto a ulamuliro wa upapa mu 1798.

Nyanga zokhala ngati za mwana wa nkhosa zikuimira kudzichepetsa, kusadzikuza komanso kudekha komwe ulamuliro wa Mgwirizano wa Maiko a ku Amerika udayamba nako. Ufulu pa ndale komanso pa chipembedzo (nyanga ziwiri) anali maziko enieni okhazikika a pfuko la Amerika. Akhristu a ku Ulaya, omwe anazunzidwa ndikuthawa ulamuliro wa papa, mu unyinji wao anapita ku "Dziko Latsopano," Amerika. Uku ndiko kudali kubadwa kwa pfuko la Amerika. Koma chirombo cha "nyanga ziwiri ngati mwana wa nkhosa" "chinalankhula ngati chinjoka." "Ndipo chichita ulamuliro wonse



wa chirombo choyamba (ufumu wa upapa) pamaso pake, ndipo chilambiritsa dziko ndi iwo akukhala momwemo chirombo choyamba… ndi kunena kwa iwo akukhala pa dziko, kuti apange fano la chirombo…" (Chibv. 13:11-14).

Maonekedwe a nyanga ziwiri ngati mwana wa nkhosa ndi kulankhula ngati chinjoka zikuimira kusiyana kwa kungolankhula mau ndi kuchita mwa ntchito. Dziko liri lonse limalankhula kudzera m'malamulo opangidwa ndi aphungu ake omwe amagwiritsidwa ntchito ndi akatswiri a za malamulo m'mabwalo a milandu (Constitution). Kuchita mosatsatira zimene zinakhazikitsidwa kumakhala kutsutsana ndi maziko oikidwa a kayendetsedwe ka dziko. Choncho ulosi wakuti chidzalankhula "ngati chinjoka" ndikuchita "ulamuliro wonse wa chirombo choyamba" ukunenera momveka bwino za kubwera kwa mtima wopanda chifundo ndi wozunza wa dziko la Amerika (Chibv.12:13,17) ngati womwe unaonetsedwanso ndi chirombo choyamba (Ulamuliro wa Upapa). Mau akuti chirombo cha nyanga ziwiri "chilambiritsa dziko ndi iwo akukhala momwemo chirombo choyamba" akuonetsa kuti ulamuliro wa pfuko la Amerika'li udzatsogolera ndi kulimbikitsa anthu kumvera



ndi kupereka ulemu ku ulamuliro wa Upapa. Lero lino tikuona momwe dziko la Amerika ndi la Vatican akugwirira ntchito molumikizana pofuna kuti chikoka chao chifalikire ponseponse.

## FANO LA CHIROMBO

Pamene mpingo woyamba unachoka m'machitidwe odzichepetsa a uthenga wabwino ndi kubvomereza miyambo ndi malangizo za chikunja, unasokonekera, kugwa ndi kusiyana nayo mphamvu ya Mulungu. Pofuna kulamulira chikumbumtima cha anthu, unafuna chithandizo cha mphamvu ya ulamuliro wachikunja. Chotsatira chake chinali ulamuliro wa upapa, womwe kudzera mwa uwu mpingo unalamulira dziko ndikuchita chiri chonse pofuna kukwaniritsa zofuna zake, monga kuzunza olungama powanamizira kuti ndi oukira. Tsono kuti Amerika apange fano la chirombo, mphamvu yachipembedzo iyeneranso kulamulira boma kuti mpata upezeke wakuti mpingo uthe kugwiritsa ntchito mphamvu za boma'lo pofuna kukwaniritsa zofuna zake.

Kudali kupandukira komwe kunatsogolera mpingo woyambawo kufuna thandizo la boma, ndipo ichi chidapereka mwai wa kukhazikitsidwa kwa ulamuliro wa upapa, "chirombo". Pofokoza za kupandukiraku Paulo akuti "Koma" chiyambe "chifike chipatukocho, nabvumbulutsidwe munthu wosayeruzika…." (2 Atesalonika 2:3-4). Monga zinachitikira kale ndimo zidzachitikiranso ndi mipingo ya mipanduko ya lero yomwe idzapereka mpata kuti fano la chirombo likhazikitsidwe. M'zaka zapita'zi kuyesetsa kukhazikitsa mgwirizano wa mipingo ya Mpanduko kwakhala kukuchitika koma "mosalingirira mwakuya za kuipa kwake" ndipo ukukhazikitsidwa ndi kulimbikitsidwa mosaganizira ngakhale za choonadi cha




Bukhu Lopatulika. M'October 1999, pakukhazikitsa Mgwirizano pakati pa Vatican ndi Luthren World Federation, bungwe'li linasonyeza kukana kwake poyera kuti zonse zimene anachita a Martin Luther za Kukonzanso (Reformation) zinali zopanda tanthauzo ndi zopanda pake pongolowa mu mgwirizanowo. Apatu zikutsimikizira kotheratu kuti bungwe la mgwirizano wa mipingo (WCC) ndi losathandiza ku uzimu woona m'za kumwamba koma ku chimpatuko chachikuru chomwe anachilosera Paulo mu 2 Atesalonika.

Pamene mipingo ikuruikuru ya dziko la Amerika, idzagwirizana pa mfundo zina ndi zina za ziphunzitso za chikunja, idzaumiriza boma kukhazikitsa malamulo okhwima pofuna kuti mipingoyo isasweke, pomwepo dziko la Mpanduko la Amerika lidzapanga "fano" la ulamuliro wa Romu, ndipo chotsatira chake chidzakhala kuzunza anthu onse amene sadzatumikira fano'lo.


Choncho, fano la chirombo mosabisa, likuimira mipingo yakugwa ya Mpanduko yomwe idzafuna thandizo la boma la dziko lapansi pofuna kukakamiza ziphunzitso zao monga unachitira ulamuliro wa Papa m'mbuyomu.

## CHIZINDIKILO CHA CHIROMBO

Chirombo chokhala ndi nyanga ziwiri (America) "chichita kuti onse…alandire chilembo pa dzanja lao ndi pamphumi pao; ndi kuti munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo kapena chiwerengero cha dzina lake" (Chibv. 13:16-17).

"Iye wakukhala nacho chidziwitso awerenge chiwerengero cha chirombocho; pakuti chiwerengero chake ndi cha munthu; ndipo chiwerengero chake ndicho mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu ndi limodzi kudza zisanu ndi chimodzi" (Chibv. 13:18).

Palibe munthu wina amene ali ndi udindo waukuru pa onse mu ulamuliro wa upapa (wotsutsana ndi chikhristu) koma Papa. Ulemu wa udindo wake umene amadziwika nao ndi




"VICARIUS FILII DEI" kutanthauza "Mlowam'malo wa Mwana wa Mulungu." (Our Sunday Visitor 4-18-1915).

M'chi – Latin dzilembo za mau zimakhala ndi ziwerengero. Ziwerengero zina za dzilembo za udindo wa Papa'wu kuziphatikiza pamodzi zimapanga chiwerengero cha chirombo chomwe ndi 666.

Pamene gulu lina la anthu lidzalandira chizindikilo cha chirombo ndi kupembedza fano lake, gulu lina likufotokozedwa kuti ndi "…iwo akusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu" (Chibv. 14:12). Choncho kusiyana kwa kupembedza koona ndi kwa bodza kukukhuzana ndi kasungidwe ka Malamulo a Mulungu komanso a Satana. Kumbali ina kuli chizindikilo cha Mulungu, kutanthauza Sabata loona lomwe limachitika pa Saturday. Pamene kumbali inayi kuli chizindikilo cha chirombo, chomwe ndi kusunga Sunday kukhala loyera. Ulamuliro wa upapa umati kusunga Sunday kukhala loyera ndi "chizindikilo cha Ulamuliro wake" chifukwa m'chaka cha 364 AD unasintha Sabata kukhala Sunday. (The Convert's Catechism, P. Geiermann).

Munthu ali yense amene wazindikira choonadi ichi koma mwadala nkumasunga malamulo osinthidwa ndi ulamuliro wa Papa'wa akulemekeza mchitidwe wokana Khristu wa iye amene wadziika kutsutsana ndi Mulungu.

Komabe pali akhristu ambiri m'mipingo yosiyanasiyana omwe akusunga Sunday, poganiza kuti pakutero akulemekeza Sabata loona la lamulo la chinai. Mulungu akuwalandirabe monga ana ake, monga kwalembedwa, "Nthawi za kusadziwako tsono Mulungu analekerera" (Machitidwe 17:30). Koma pamene kusunga kwa Sunday mu nthawi ino ya kukhazikitsidwa kwa "Kayendetsdwe Katsopano ka Dziko Lapansi (New World Order)," komwe kwayambira ku America kudzakhala kokakamiza mwa lamulo, dziko lapansi litalalikidwa kwa nthawi yaitali za Sabata loona, ndipo onse omwe mwadala adzasankha kuswa lamulo la Mulungu ndi kusunga Sunday, nthawi yomweyo adzalandira chizindikilo cha chirombo. Otero'wo asayembekezerenso chisomo cha Mulungu koma mkwiyo




wake ndi chilango cha imfa ya myaya. (Chibv. 14:9-11). Momwe anthu azunzidwire mu nthawi ya kukakamiza kwa lamulo la Sunday zinakhazikitsidwa kale ndi bungwe lija la Mipingo yonse ya Dziko lapansi (World Council of Churches) atsogoleri a maiko komanso bungwe la Mgwirizano wa Maiko (United Nations) ku New York. Cholinga ndicho kupanga chipembedzo chotsutsana ndi Bukhu Lopatulika cha Tsiku la Sunday monga momwe ulamuliro wa Upapa mogwirizana ndi mgwirizano wa zipembedzo ukufunira. Kuyendera kowirikiza kwa maiko ndi maboma osiyanasiyana komwe Papa akukuchita, makalata ake a uepiskopi ndi zonse zimene akuchita zokhuza dziko lapansi'li zikungolimbikitsa chikonzetsero ichi.

## NANGA CHISANKHO CHANU NDI CHOTANI?



ZOCHITIKA ndiponso ngozi zakugwa mwadzidzidzi m'dziko lapansi lero lino zikhala zikuchurukira churukira kufikira kubwera kwa Khristu. Pamene dziko lapansi loipa'li ndi ntchito ziri momwemo lidzaonongedwa, Mulungu "afuna anthu onse apulumuke, nafike pozindikira choonadi." "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha" (1 Timoteo 2:4; Yohane 3:16).

Motsutsana ndi zolingalira za dziko lapansi, Mulungu akulonjeza tsogolo la ulemelero woposa kwa iwo amene akuchita chifuniro chake pa dziko lapansi pano: "Pakuti taonani, ndilenga kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano; ndipo zinthu zakale sizidzakumbukika, pena kulowa mu mtima." "Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuichotsa pamaso pao; sipadzakhalanso imfa; sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena chowawitsa; zoyambazo zapita … Taonani, ndichita zonse zikhale zatsopano" (Yesaya 65:17; Chibv. 21:4-5).

Mau awa sakupatsa chiyembekezo za moyo wa mtsogolo wokha ai, koma akupatsanso mtendere ndi chilimbikitso m'moyo uno.

Chiweruziro chikuchitika kumwamba panopo. Posachedwa –ingakhale palibe akudziwa bwino bwino za kufulumira kwa nthawiyo – mulandu wa munthu ali yense udzaweruzidwa. Choncho, ndi kofunikira kuti munthu ali yense alitenge chenjezo ili motsimikizika mu mtima mwake: "Lero ngati mudzamva mau ake, musaumitse mitima yanu" (Ahebri 3:7-8). Pamene ntchito ya chiweruziro cha kufufuza idzatsekedwa, munthu aliyense adzakhala akudziwa mbali imene ali - ku moyo wosatha kapena ku imfa. Chitetezero cha dziko lapansi chitsekedwa mwadzidzidzi Yesu Khristu asanaonekere m'mitambo ya kumwamba.

Yesu Khristu anafa pa mtanda pa Gologotha chifukwa cha machimo ako pofuna kukutsegulira njira ya ku moyo ulinkudza wa ulemelero. Ingakhale panopa ungathe kudza kwa Iye m'pemphero, utalapa machimo ako ndi kuyamba moyo watsopano pokuchita malamulo ake. Ndipo Iye adzapitiriza kukupembedzera pa nthawi yonse ya chiweruziro.

**RLMedia**
32 Ceres Str, Comptonville,
Johannesburg, South Africa
www.rlmedia.co.za
+27(0)836254786